
KHONSOLO YA MZINDA
WA LILONGWE

# NDONDOMEKO YAKAGWIRIDWE KA NTCHITO

Kuyambira mchaka cha **2020** mpaka **2025**






## LILONGWE

**MZINDA WA UKHONDO, OSAMALA CHILENGEDWE KOMANSO OTUKUKA**

# ZAMKATIMU


MAU A MFUMU YA MZINDA WA LILONGWE — 03

MAU OCHOKERA KWA MKULU WA KHONSOLO YA MZINDA WA LILONGWE — 04

LILONGWE: MZINDA WATHU — 05

GAWO LOYAMBA: ZACHUMA — 07

| | | |
|---|---|---|
| 1.1 | Kukhala ndi ndondomeko yachuma yomveka bwino, yowunikira mozama zinthu zofunikira yomwe ingabweretse zotsatira zabwino pofuna kuonetsetsa kuti K80 pa K100 iliyonse ya mundondomekoyi ikupita kuntchito zopindulira anthu amumzindawu pofika mchaka cha 2024/25 | 08 |
| 1.2 | Kukweza ntchito zotolera ndalama zokwana 47 biliyoni kwacha pofika mchaka cha 2025 | 08 |
| 1.3 | Kuchepetsa ngongole zonse ndicholinga chopititsa ndalama zina kuntchito zachitukuko zikuluzikulu ndikukonza zinthu zakale | 09 |
| 1.4 | Kubwezeretsa chikhulupiliro pakati pa anthu kudzera pakayendetsedwe kabwino kachuma | 09 |

GAWO LACHIWIRI: KAGWIRIDWE KANTCHITO — 10

| | | |
|---|---|---|
| 2.1 | Kusintha kachitidwe ka zinthu ndi kulimbikitsa ulamuliro wabwino | 11 |
| 2.2 | Kupereka ntchito 38 zopindulira anthu amumzinda wa Lilongwe kudzera mu ndondomeko ya mgwirizano ndi makampani. | 12 |
| 2.3 | Kupeza ndalama zokwana K5 biliyoni kudzera mumgwirizano ndi mabungwe akunja komanso mabunwe omenyera ufulu wa anthu. | 13 |
| 2.4 | Kukonzanso ntchito za Khonsolo, kuthetsa mchitidwe wojomba pantchito komanso chinyengo pamalipilo | 14 |
| 2.5 | Kukhazikitsa njira younika mmene anthu akugwirira ntchito | 14 |

GAWO LACHIWIRI: KUPEREKA NTCHITO KWA ANTHU — 15

| | | |
|---|---|---|
| 3.1 | Kukweza chuma ndi kuthandiza magulu azamalonda omwe sali mkaundula waboma okwana 1, 600 | 16 |
| 3.2 | Kukulitsa malo ndi ndikuteteza zachilengedwe | 16 |
| 3.3 | Kuchotsa ndi kutaya zinyala ku malo oyenera | 17 |
| 3.4 | Kukhala ndi misewu yabwino ndi yamakono | 17 |
| 3.5 | Kuchepetsa mlili wa Covid-19, kulimbikitsa ntchito za umoyo, chisanmaliro cha ana ndi uchembere wabwino | 18 |
| 3.6 | Kuthandiza mabanja okwana 25,000 kukhala ndi nyumba, malo ovomerezeka ndi kutsilizitsa ndondomeko zinayi za chitukuko | 18 |
| 3.7 | Kupeza ndalama ndi kukhazikitsa ntchito ya chitukuko yokwana $20 million | 19 |
| 3.8 | Kukweza ntchito zamaphunziro popeleka thandizo la ndalama kuchekera kuthumba la Khonsolo zokwana K400million | 19 |
| 3.9 | Kupezera ntchito kwa achinyamata zokwana 10,000 ndikubweretsa mipikisano yosiyanasiyana kwa anthu okwana 50,000 | 20 |


Khonsolo ya mzinda wa Lilongwe

# MAU **A MFUMU YA MZINDA WA LILONGWE**

Ndiri onyadira kukhala Mfumu ya Mzinda wa Lilongwe omwe ndi okongola kwambiri komanso ndi likulu la dziko la Malawi. Mzindawu uli ndikuthekera kochita zinthu zapamwamba chifukwa uli ndi anthu amphamvu komanso aluso losiyanasiyana.

Cholinga chathu chachikulu mumzinda muno ndi **'kutumikira anthu okhala mu mzinda wa Lilongwe'** ndipo masophenya athu ndi **'kukhala ndi mzinda wa ukhondo, osamala chilengedwe komanso otukukuka'.** Pogwira ntchito yathu tidzatsatira msanamira izi: kugwira ntchito molimbika, mwangwiro, motumikira anthu, kubweretsa zotsatira zabwino kwa nzika ndi kulimbikitsa luso latsopano.

Ngakhale zili chonchi mzindawu uli pampanipani chifukwa cha mavuto a zachuma ndipo ndikofunika kuti tipeze njira yothetsera mavuto amenewa ndi cholinga chobwezeretsa chuma cha khonsoloyi mchimake.

Mavuto azachuma amenewa akhudza kwambiri kuthekera kwathu kopereka ntchito zoyenera kwa anthu okhala mu mzinda wathu. Monga zipatala zathu zilibe ogwira ntchito okwanira, misewu yathu yambiri ilibe magetsi komanso simakonzedwa kawirikawiri. Kuonjezera apo, tikulephera udindo wathu ogwira ntchito ndi makampani omwe ndi ofunika kwambiri pantchito zokweza chuma cha mzinda uno.

Ndalama zomwe timapeza zimangokwanira kulipira anthu athu ogwira ntchito ndi kuyendetsera ntchito za mmaofesi popanda zotsala kuti tiyambitsire ntchito zina zachitukuko.

Kuonjezera apo, khonsoloyi ili ndi ngongole zambiri zomwe zikupitilira ndalama zomwe imapeza pachaka. Ndalama zomwe khonsolo ikupeza pachaka zikuthera kubwezera ngongole zamgonagona. Zipangizo zathu zogwilira ntchito ndi zakalekale ndipo zimafuna kukonzedwa pafupipafupi.

Kuzemba kulipira misonkho, ziphuphu ndi kusayendetsa bwino ntchito za mmaofesi ndi zina mwa zomwe zikuthandizira kukolezera mavuto azachuma omwe mzinda wathu ukukumana nawo.

Ngakhale tikukumana ndi mavuto amenewa, khonsoloyi ikhazikitsa njira zokhwima ndi zodalirika ndi cholinga chobwezeretsa chuma chake mchimake. Zina mwa njirazi ndi; kukonzaso kayendetsedwe kandondomeko yazachuma; kutolera ndalama zambiri; kuyendetsa bwino ngongole ndi katundu wa khonsolo, kuchita zithu moyenera komanso poyera.

Mkatikati mwa chaka cha 2019 khonsolo inalemba akuluakulu oyendetsa ntchito za khonsolo atsopano, ngakhale akuluakulu amenewa anabweretsa njira zofuna kusitha kayendetsedwe kantchito zoyendetsera khonsolo yathu, magwiridwe athu antchito adakali achikalekale. Mwachitsanzo mpaka pano ogwira ntchito anthu akugwiritsa ntchito manja kutchetcha, kukonza mu ngalande ndi kusesa. Pofuna kubweretsa kusitha ndipofunika kuwonetsetsa kuti anthu athu ogwira ntchito komanso chiwerengero cha ogwira ntchito chiyenderane ndi ntchito yomwe ilipo.



## Juliana G. Kaduya

Izi zithandiza kusitha kuchoka ku khonsolo yongolemba anthu ntchito kufika ku khonsolo yolemba anthu odziwa ntchito. Komanso kukhala khonsolo yomwe zina mwa ntchito zake zidzagwiridwa ndi makampani ena poonetsetsa kuti ntchitozi zikugwiridwa pogwiritsa njira zamakono.

Ndondomeko iyi ibweretsa kusintha kwakukulu komwe kudzathandizire kulimbikitsa kusunga mwambo pantchito komanso kupanga ziganizo zofunikira. Kuti zonsenzi zitheke pakufunika kudzipereka ndi kulimba mtima pakati pa anthu ogwira ntchito poganizira kuti pali zotsamwitsa zambiri zomwe Khonsoloyi ikukumana nazo

Ine ndiwokhutira kuti tikwaniritsa **masophenya** athu ndiponso tibwezeretsa chikhulupiliro chomwe munali nacho mu khonsolo yanu.

Juliana Kaduya

**Mfumu ya Mzinda wa Lilongwe**



Translated and designed by the Department of Information

# MAU OCHOKERA KWA **MKULU WA KHONSOLO YA MZINDA WA LILONGWE**



## John Chome

Kwa zaka zambiri Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe yakhala isakuchita bwino pakagwiridwe kantchito zake. Anthu okhala mu mzindawu, mabungwe ndi makampani omwe timagwira nawo ntchito anataya chikhulupiliro ku khonsoloyi chifukwa cha momwe timagwilira ntchito. Pofuna kuyamba mwatsopano ngati khonsolo, tinagwirizana kuti tibwezeretse chikhulupiliro chomwe anthu anali nacho ku khonsolo posintha kagwiridwe ndi kachitidwe kazinthu.

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe yakhazikitsa ndondomeko yapamwamba yomwe ndi yazaka zisanu kuyambira mchaka cha 2020 kufika mchaka cha 2025 ndi cholinga chositha mzindawu.

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe yakhazikitsa ndondomeko yakagwiridwe kantchito ya zaka zisanu. Ndondomekoyi yomwe ndi yapamwamba kwambiri cholinga chake ndikufuna kusitha zinthu mu mzindawu ndipo ikuyamba mchaka cha 2021 mpaka mchaka cha 2025.

Ndondomekoyi yabwera munthawi yoyenera pamene dziko la Malawi lakhazikitsa masophenya achitukuko a 2063. Imodzi mwa msanamira zitatu yamasophenya a 2063 ndi kukhala ndimalo amakono omwe adzakhale ndichito zachitukuko zosiyanasiyana komanso misika zomwe zidzapezetse anthu mwayi wa ntchito. Ndondomeko ya Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe ithandizira kukwaniritsa masophenya a 2063. Ndondomekoyi idzathandiziranso kusitha pakagwiridwe kantchito za khonsolo kuti zibweretse zipatso zabwino zokomera anthu okhala mumzindawu.

Choyenera kudziwa ndi chakuti ndondomekoyi inakonzedwa potenga maganizo a anthu ambiri ndikugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyanasiyana panthawi yomwe dziko la Malawi liri pakati polimbana ndi muliri wa Covid-19. Pachifukwa chimenechi ndati ndithokoze anthu onse amene anatenga now gawo kupereka nzeru ndi maganizo awo ndi cholinga chopanga Lilongwe kukhala Mzinda wapamwamba mdziko muno.

Ndondomekoyi idzapangitsanso kuti ntchito zofunikira ziperekedwa kwa anthu okhala mumzindawu pokhazikitsa njira zapamwamba zoyendetsera ntchito za khonsolo. Ndondomekoyi yagawidwa mmagawo atatu omwe ndi kupititsa patsogolo ntchito zachuma, kusitha kagwiridwe kantchito kamakono kulimbikitsa kupereka ntchito zapamwamba kwa anthu okhala mu mzindawu.

Ndondomekoyi ndiyofunikira kwambiri, pachifukwa ichi, Khonsoloyi ndiyomasuka kulandira maganizo ena aliwonse ochokera kwa anthu okhala mumzindawu, ochita zamalonda, mabungwe omenyera ufulu wa anthu ndi ena onse okhudzidwa pa momwe ndondomekoyi ikuyendetsedwera.

Pofuna kuonetsetsa kuti ndondomekoyi ikutsatiridwa, khonsolo idzakhazikitsa nthambi yapadera yomwe izidzaunika mmene ntchito zikugwiridwira chaka china chirichonse. Ndondomekoyi iyendetsedwa mogwirizana ndi lonjezo lathu latsopano lakagwiridwe kantchito.

Ine ndiri ndi chikhulupiliro kuti pakugwilira ntchito limodzi tipanga mzinda wa Lilongwe kukhala waukhondo, wosamala chilengedwe komanso otukuka.

John Chome

**Mkulu oyendetsa ntchito za Mzinda wa Lilongwe**



Translated and designed by the Department of Information


# **LILONGWE:** MZINDA WATHU

LILONGWE ndi mzinda waukulu ku Malawi omwe udayamba ngati mudzi waung'ono wa asodzi a nsomba mumtsinje wa Lilongwe. Atsamunda anakhazikitsa Lilongwe kukhala Boma mchaka cha 1902 pomanga linga pafupi ndi mtsinje wa Lilongwe. Mchaka cha 1965, chiganizo chosamutsa likulu la dziko la Malawi kuchoka ku Zomba kupita ku Lilongwe komwe ndi pakatikati pa dziko lino chinapangidwa ndi cholinga chakuti ntchito zachitukuko zifalikire madera onse a dziko lino mosavuta. Mchaka cha 1975 Lilongwe anakhazikitsidwa kukhala likulu latsopano la dziko la Malawi kudzera mu lamulo la Nyumba ya Malamulo.

Kutsatira kusamutsidwa kwa malikulu amaunduna onse aboma mchaka cha 2005 kunachititsa kuti chiwerengero cha anthu okhala mu mzinda wa Lilongwe chikwere kwambiri. Lilongwe, kukhala mzinda wadongosolo, unagawidwa mmagawo anayi omwe ndi: Old-Town, Capital Hill, Kanengo ndi Lumbadzi. Chikonzero chimenechi chinakhazikitsa malo okhala anthu, malo ogwira ntchito ndi malo antchito zamalonda. Izi zinakhazikitsidwa ndi cholinga chofuna kuchepetsa mtunda omwe anthu angamayende popita kumalo antchito kapena amalonda komanso kuchepetsa kuthithikana kwa anthu.
Kuwonjera pamenepa, mzindawu unagawidwa mmagawo ang'onoang'ono 58 omwe amadziwika kuti ma Area. Boma la Lilongwe likupezeka mchigawo chapakati ndipo ndi limodzi la maboma akuluakulu mdziko lino.

Boma la Lilongwe momwe mzindawu ukupezeka linakhazikika mdera lomwe limadziwika ndi ntchito za ulimi kuyambira kale lonse ndipo ndikumene kumapezeka msika wa mbeu zosiyanasiyana monga fodya, chimanga, mtedza, soya ndi zina zambiri. Ntchito zomwe zimabwereta chuma pakati pa anthu amumzindawu ndi monga izi; zomangamanga, ntchito zaboma, zokopa alendo, malonda a fodya ndi ntchito za mafakitale.

Mumzindawu mukupezekanso bwalo la ndege lalikulu la Kamuzu lomwe likupezeka cha kumpoto kwa mzindawu ndipo anthu opitilira 600,000 ndiomwe amakwera ndege chaka chirichonse.
Kafukufuku wathu akuonetsa kuti mwa anthu 27 pa 100 aliwonse amagwira ntchito mboma, 40 mwa anthu 100 amagwira ntchito mmakampani pamene anthu 24 mwa 100 aliwonse amagwira ntchito yodzilemba okha.
Chiwerengero cha anthu mu mzinda wa Lilongwe chikudutsa pa 1 miliyoni komanso chikukwera mofulumira. Kuwonjezera pamenepa, chiwerengero cha anthu osauka komanso omwe sakugwira ntchito ndichokwera.




| ZAKA | CHIWELENGERO CHA ANTHU |
|---|---|
| 1966 | 19,425 |
| 1977 | 98,718 |
| 1987 | 223,318 |
| 1998 | 440,471 |
| 2008 | 674,448 |
| 2015 | 905,000 |
| 2020 | 1,122,000 |


Translated and designed by the Department of Information

# MAU **OYAMBA**

Ndondomeko iyi ikulongosola za momwe Mzinda wa Lilongwe ungapitire patsogolo ndi ntchito zake kuyambira mwezi wa Julaye mchaka cha 2020 mpaka mwezi wa Juni mchaka cha 2025.

Maboma ang'ono anakhazikitsidwa kudzera mu Gawo 146 la Malamulo akulu a dziko lino. Gawoli limafotokoza kuti okhawo osankhidwa ndi anthu ndi amene ali ovomerezekeka kuyimirira madera awo ndi cholinga chofuna kukwaniritsa izi;

**Kukweza ntchito za mabungwe a maufulu a anthu ndi kulimbikitsa anthu kutenga nawo gawo pa zochitika za madera awo**

**Kulimbikitsa ntchito za chitukuko cha chuma ndi zomangamanga**

**Kulimbitsa ntchito za makampani pa ntchito za chitukuko**

**Kukweza ntchito zophunzitsa anthu zinthu zomwe zikuwakhudza ngati mkhala pakati wa boma ndi anthu**

Pofuna kukwaniritsa udindo opereka ntchito zoyenera kwa anthu amumzindawu, tikuyenera kukhala osinthika muzochita zathu. Kulephera kuchita izi zidzapitiriza kuchotsa chikhulupiliro chomwe chilipo pakati pa anthu ogwira ntchito ku khonsolo, anthu okhala mu mzindawu ndi magulu ena ogwira nawo ntchito. .

Pali zifukwa zakwanira kuti khonsolo yathu iri ndikuthekera kwakuti ikhoza kusinthika ndikuyambanso kupereka ntchito zonse zofunikira zomwe anthu okhala mu mzindawu amayenera kulandira.

Palinso kuthekera kwakukulu kwakuti katoleredwe ka misonkho katha kupita patsogolo zomwenso zithandize kupititsa patsogolo mgwirizano wa khonsolo ndi makampani ogwira nawo ntchito ndi cholinga chopititsa patsogolo kupereka ntchito zofunika kwa anthu okhala mu mzindawu.

Khonsoloyi iri ndi abwezi omwe ali okonzeka kuthandiza kusintha kugwiridwe ka ntchito zake ndipo Unduna wa Maboma Ang'ono uli ndi chidwi choonetsetsa kuti khonsoloyi ikukwaniritsa masomphemya ake. Banki lalikulu la Dziko Lonse (World Bank) ndi limodzi mwa mabungwe omwe awonetsa chidwi chofuna kugwira ntchito limodzi ndi khonsoloyi ndipo pali chiyembekezo chakuti mabungwe ena achitanso chimodzimodzi ngati khonsoloyi ingabweretse zipatso zabwino. Chinthu china ndi chakuti anthu okhala mumzindawu ndi magulu ochita zamalonda ali ndi chidwi chofuna kutenga nawo mbali pantchito yofuna kusintha kagwiridwe kantchito ka mumzindawu

## CHOLINGA CHACHIKULU

Kutumikira anthu okhala Mumzinda wa Lilongwe ndi mtima onse

## MASOMPHENYA

Kukhala Mzinda wa Lilongwe wa ukhondo, osamala chilengedwe komanso otukuka

## ZIKHULUPILIRO ZATHU

Ngodya zathu zimaonetsa zikhulupiriro zathu, chomwe ife tili ngati bungwe. Izi ndi zomwe zimatithandiza kugwira ntchito molondora. Ngodya zathuzi timazitsatira muchirichonse chomwe timachita. Zina mwangodyazi ndi izi;

**Kulimbikira ntchito podzipereka ndikugwira ntchito iliyonse mwa ukadaulo**



Translated and designed by the Department of Information

Kukhala ndi umunthu odzipereka, okhulupirika pogwira ntchito

Kutsogoza ntchito zimene khonsolo imapereka kwa anthu okhala mu mzindawu

Kukhazikitsa ntchito zooneka zimene anthu okhala mu mzinda wa Lilongwe angakhutitsidwe nazo

Kulimbikitsa nzeru zakuya ndi luso la kagwiridwe kantchito kamakono

# **KULONGOSOLERA** NDONDOMEKO

Mwachidule, iyi ndi ndondomeko yakagwiridwe kantchito za khonsolo ya mzinda wa Lilongwe yomwe yakonzedwa ndi cholinga chakuti anthu okhala mu mzindawu athe kudziwa zomwe khonsolo yawo ingawapangire.

Ndondomekoyi irii mmagawo atatu amene ndi zachuma, kayendetsedwe kantchito za khonsolo ndi ntchito yopereka zithu zofunikira kwa anthu okhala mu mumzindawu. Magawo awiri oyambilirawa akhazikika popititsa patsogolo ntchito zachuma, zaumoyo ndi zakayendetsedwe ka khonsoloyi zomwe ndi maziko a ntchito yopereka zinthu zofunikira kwa anthu okhala mu mzindawu.

Gawo lirilonse liri ndi cholinga chachikulu komanso likumagawidwa mmagawo ena ang'onoang'ono. Ndondomekoyi ili ndi magawo ang'onoang'ono okwana 17 zothandiza kukwaniritsa masophenya a Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe. Mndandanda wa ndonomekoyi wakonzedwa kuti uthe kufotokonzera mwachidule mmene zinthu ziliri mu mzindawu, mfundo zofotokoza mmene khonsoloyi igwirire ntchito zake komanso ntchito zikuluzikulu zimene khonsoloyi yakonza kuti igwire ndi kukwaniritsa.

Izi zithandiza anthu amene awerenge ndondomekoyi kukhala ndi chithunzithunzi cha mmene zinthu ziliri ndi zimene khonsoloyi yakonza kuti ichite potukula mzinda wa Lilongwe.



Translated and designed by the Department of Information

# GAWO LOYAMBA: **ZACHUMA**

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe ili mmavuto azachuma chifukwa chakuchepa kwa njira zopezera ndalama zoyendetsera ntchito zake. Pachifukwa chimenechi, ntchito zofunika zomwe khonsoloyi imapereka kwa anthu zikuwerengedwa pamulingo wa 11 Kwacha pa tsiku pa munthu aliyese okhala mumzindawu. Izi zikupangitsa kuti Khonsolo ilephere kupereka ntchito zachitukuko zolozeka kwa anthu. Zambiri mwa ndalama zomwe mzindawu umapeza zimangogwiritsidwa polipira anthu ogwira ntchito ndikuyendetsera ntchito za Khonsoloyi zomwe zimapangitsa kuti pasamakhale ndalama zokwanira pantchito yachitukuko cha zomangamanga.

Kuwonjezera pamenepa, Khonsoloyi ili ndi ngongole zochuluka zomwe zikupangitsa kuti ndalama zomwe ikadagwiritsa pantchito zina zachitukuko zidzikuthera kubweza ngongole zamgonagona. Katundu wambiri wa Khonsoloyi monga magalimoto ndi nyumba zogwilira ntchito ndizakale zomwe zimafunika kukonzedwa pafupipafupi. Izi ndizomwe zikuchititsa kuti ntchito zofunika zomwe Khonsoloyi imapereka kwa anthu izitenga ndalama zambiri. Kuzemba kulipira msonkho, ziphuphu ndikusayendetsa bwino ntchito za Khonsolo ndi zomwenso zathandizira kuti ntchito zachuma zikhale zisakuyenda bwino kwa zaka zambiri.

Pofuna kuthetsa mavuto amenewa Khosoloyi itsata njira zosiyanasina monga; kusitha kakonzedwe kandondomeko ndi kayendetsedwe kachuma, kupeza njira zothandizira kutolera ndalama zochuluka, kuonetsetsa kuti ngongole za Khonsolo zikulipidwa moyenera komanso katundu akusamalidwa bwino. Kuwonjezera pamenepa, Khonsolo idzaonetsetsa kuti ndalama zake zikugwira ntchito moyenera ndi mosabisa kanthu. Njira ina, khonsolo idzalimbikitsa magawo onse a zowunika ndalama ndicholinga chakuti ndondomeko ya ndalama ithandizire ogwira ntchito kupanga ziganizo zoyenelera zomwe zidzapindulire anthu okhala mumzindawu.

## Cholinga chachikulu

Kukonzanso chuma cha Khonsolo, powonjezera njira zotolera ndalama, kuzipititsa kumagawo oyenera ndikuyendetsa bwino chuma ndi kuonetsetsa kuti ndalama zikupita ku magawo ofunikira kwambiri omwe angapindulire anthu okhala mumzinda wa Lilongwe.

## Zolinga zazing'ono

**Ndondomeko ya chuma**

**Kutolera ndalama**

**Katundu ndi ngongole**

**Kuunika mozama**





Translated and designed by the Department of Information

## 1.1 Kukhala ndi ndondomeko yachuma yomveka bwino, yowunikira mozama zinthu zofunikira yomwe ingabweretse zotsatira zabwino pofuna kuonetsetsa kuti K80 pa K100 iliyonse ya mundondomekoyi ikupita kuntchito zopindulira anthu amumzindawu pofika mchaka cha 2024/25

Kutengera mbiri ya ndondomeko ya zachuma, ndalama zambiri zakhala zikupita kumagawo oyendetsera ntchito za mmaofesi akhonsolo mmalo mopita kuntchito zopindulira anthu amumzindawu. Kawirikawiri ndondomeko ya zachuma simawonetsa bwino lomwe ndalama zomwe zimapita kuntchito zothandiza anthu. Izi ndizomwe zimalepheretsa khonsolo kudziwa ndalama zomwe zingapite kumagawo antchito zothandiza anthu okhala mumzinda. Pofuna kukonza izi, Khonsolo itsata njira zinayi izi:

1.1.1 Kukhazikitsa njira yabwino ya kayendetsedwe kachuma pofuna kuchepetsa ndalama zogwiritsa ntchito poyendetsa maofesi, kuteteza ntchito zopindulira anthu amumzindawu, kupeza katundu ofunikira ndiponso kubweza ngongole.

1.1.2 Kukhazikitsa mulingo wa ndalama zomwe Khonsolo ingatolere mogwirizana ndi malamulo.

1.1.3 Kulimbikitsa kuchita zinthu poyera poyendetsa ndondomeko ya zachuma.

1.1.4 Kulimbikitsa nzeru zatsopano zakagwiridwe kantchito powonjezera ndalama zogwilira ntchito.

## 1.2 Kukweza ntchito zotolera ndalama zokwana 47 biliyoni kwacha pofika mchaka cha 2025

Khonsolo ya mzinda wa Lilongwe ili ndi njira zochepa zotolelera ndalama zothandizira anthu okhala mumzindawu. Mchaka cha 2018/19 ntchito zofunika zomwe khonsoloyi imapereka kwa anthu zimawerengedwa pamulingo wa 11 kwacha pa tsiku pa munthu aliyese okhala mumzindawu. Kutolera kwa ndalama kukukumana ndi mavuto monga kusowa njira zolimbikitsa kutolerara ndalama, ziphuphu ndikusayendetsa bwino ntchito za Khonsolo. Pofuna kukonza izi, Khonsolo itsata njira zisanu ndi imodzi izi:

1.2.1 Kukhazikitsa njira zolimbikitsira otolera ndalama; kutengera ku khoti anthu ozemba kulipira msonkho; kulimbikitsa adindo kutengapo gawo; kulimbikitsa ntchito yotolera ndalama za msonkho wakatundu zokwana 7 billiyoni mwa ndalama 11 biliyoni zomwe zili mu anthu ndi makampani

1.2.2 Kuwonjezera magawo omwe angathandizire ntchito yotolera msonkho pogwiritsa luso lomwe mabungwe ena amatsata

1.2.3 Kulimbikitsa kasungidwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka kaundula potolera ndalama

1.2.4 Kupereka ntchito yotolera ndalama kwa anthu amalonda ndikusamala katundu wa Khonsolo

1.2.5 Kukonzanso kagwiridwe kantchito kanthambi za Khonsolo poyika mulingo wa katoleredwe ka msonkho pa akuluakulu onse

1.2.6 Kufewetsa ndondomeko zotolera ndalama; kukhala ndi mulingo umodzi ofanana komaso kuthetsa misonkho yopanda pake

## 1.3 Kuchepetsa ngongole zonse ndicholinga chopititsa ndalama zina kuntchito zachitukuko zikuluzikulu ndikukonza zinthu zakale

Khonsolo ya mzinda wa Lilongwe ikukumana ndi mavuto azachuma ankhaninkhani ndipo pofika mchaka cha 2018 ngongole zomwe khonsolo inali nazo zinafika podetsa nkhawa. Mwachitsanzo, khonsoloyi inali ndi ngongole ya 700 miliyoni kwacha yoti ilipire ku makampani, 1.8 biliyoni yolipira kwa anthu ogwira ntchito ngati chipukuta misonzi ndi 1.5 biliyoni ya misonkho ya anthu ake apantchito.


Translated and designed by the Department of Information

Pachifukwa chimenechi, panalibenso ndalama zoyambitsira ntchito zachitukuko zikuluzikulu ndipo magalimoto ndi zida zonse zogwilira ntchito zinali zitatha nthawi yake.

1.3.1 Kukhazikitsa thumba lapadera la ndalama zolipilira anthu onse omwe akupuma ndi kuchotsedwa ntchito

1.3.2 Kumaliza kulipira ngongole yonse ku banki ya FDH komanso kupitiliza kulipira ngongole ya TEVETA ndi ngongole ya anthu ogwira ntchito malinga ndi mgwirizano omwe ulipo ndi bungwe lotolera misonkho mdziko muno (MRA).

1.3.3 Kukhazikitsa thumba lapadera lothandizira kupeza ndi kusamalira katundu wa khonsolo watsopano.

## 1.4 Kubwezeretsa chikhulupiliro pakati pa anthu kudzera pakayendetsedwe kabwino kachuma

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe imayang'anira ndalama mmalo mwa anthu okhala mumzindawu. Zaka zammbuyomu khonsoloyi yakhala ikulephera udindo wake ogwiritsa ntchito ndalama. Mwachitsanzo, kuchokera mchaka cha 2012 kufika mchaka cha 2018 sipanachitike kawuniwuni wina aliyense wa momwe ndalama zinagwiritsidwira ntchito. Mmbuyomu mabuku a ndalama samaperekedwa munthawi yake kubungwe la boma lowona kayendetsedwe kachuma cha makhonsolo la National Local Government Finance Committee. Khonsoloyi inalibenso ndondomeko yakagulidwe ka katundu ndipo imalephera kupereka malipoti ku bungwe la boma lowona za kagulidwe ndi kugulitsidwe ka katundu wakale la Public Procurement and Disposal of Assets Authority.

Zofooka izi zimasokoneza ubale ndi chikhulupiliro pakati pa khonsoloyi ndi boma, mabanki ndi mabungwe ena azachitukuko.

### Zotsatira zoyembekezereka Chaka chirichonse

1. Nthambi ya Kalondolondo wa zachuma cha Boma idzapereka zotsatira zakauniuni wachuma zomwe khonsoloyi idzakambirane ndikukonzanso zolakwika

2. Kuonetsetsa kuti malipoti ofunikira aperekedwa ku bungwe la boma lowona zakayendtsedwe kachuma cha mmakhonsolo ndi nthambi yawona zogula ndikugulitsa katundu wa boma

3. Kuonetsetsa kuti nthambi ya kalondolondo wachuma cha khonsolo ili ndi anthu ogwira ntchito okwanira

4. Kuonetsetsa kuti nthambi ya kalondolondo wachuma cha khonsolo ikupereka zotsatira zakauniuni mwezi uliwonse


Translated and designed by the Department of Information

# GAWO LACHIWIRI: **KAGWIRIDWE KANTCHITO**

Mchaka cha 2019, Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe inalemba anthu ogwira ntchito amaudindo akulakulu. Ngakhale amenewa anabweretsa kachitidwe katsopano pakagwiridwe kantchito, khonsoloyi ikupitiliza kugwira ntchito zake mwachikale monga mmene zinaliri poyambilira. Khonsoloyi iri ndi anthu ambiri omwe ntchito yawo ndi kungotumikira mmaofesi. Komanso mpaka pano anthu ogwira ntchito akugwiritsabe ntchito manja potchetcha tchire, kusesa ndi kukonza mungalande.

Pofuna kusintha zimenezi, ndikoyenera kuti ogwira ntchito adzipereka malipoti olongosola momwe akugwilira ntchito yawo. Izizithandiza kusitha kuchoka ku khonsolo yongolemba anthu ntchito kufika ku khonsolo yolemba anthu odziwa ntchito potengera ntchito yomwe ilipo. Komanso kukhala khonsolo yomwe zina mwantchito zake zidzagwiridwa ndi makampani ena. Khonsoloyi idzaonetsetsanso kuti ikutsata njira zamakono poyendetsa ntchito zake komanso iyesetsa kukhazikitsa ubale ndi makampani, mabungwe omenyela

## Cholinga chachikulu

Kugwira ntchito mwaluso, kulimbikitsa ntchito za makampani, kukhazikitsa ubale, kulimbikitsa ulamuliro wabwino, kupereka ntchito kwa anthu munthawi yoyenera komanso kuchita zinthu poyera.

## Zolinga zazing'ono

2.1 Ulamuliro wabwino

2.2 Kukhazikitsa ubale ndi makampani

2.3 Kulimbikitsa ubale pogwira ntchito za chitukuko

2.4 Kukonza ndi kusintha kagwiridwe ka ntchito

2.5 Kukhazikitsa njira zothandiza kuunika momwe anthu akugwilira ntchito

## 2.1 Kusintha kachitidwe ka zinthu ndi kulimbikitsa ulamuliro wabwino

ufulu wa anthu, mabungwe ogwira ntchito zachitukuko ndi boma.

Kusintha kachitidwe ka zinthu ndi kulimbikitsa ulamuliro wabwino ndikofunikira pofuna kupititsa patsogolo ntchito za Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe. Pofuna kuonetsetsa kuti kusinthaku kukuchitika mwa dongosolo, ndikofunika kuunika nkhani zonse zokhuza ulamuliro wabwino pochita izi:

1. Kuonetsetsa kuti makhansala akupatsidwa upangiri kuti adzitha kugwira ntchito yawo yopanga lamulo ndi kuimilira anthu ammadera awo pa ntchito zichitukuko bwino.

2. Kuonetsetsa kuti anthu ochuluka akutenga nawo gawo pa zokambirana zokhuza kukweza miyoyo yawo.

3. Kulimbikitsa amayi ndi achinyamata kukhala pa maudindo akuluakulu oyendetsa ntchito za khonsolo.

### Njira zokwana zisanu ndi ziwiri (7) zakonzedwa pofuna kusintha kachitidwe ka zinthu ndi kulimbikitsa ulamuliro wabwino;

2.1.1 Kulimbikitsa utsogoleri wa masomphenya ndi chikhalidwe chodzipereka pa ntchito

2.1.2 Kupereka mwayi kwa anthu opereka maganizo awo pa ntchito zachitukuko zomwe akuzifuna

2.1.3 Kukhazikitsa ofesi yoima payokha yomva madandaulo a anthu ngati njira imodzi yolimbana ndi katangale

2.1.4 Kukhazikitsa thumba lapadera lomwe lidzithandiza makhansala kugwira ntchito yowunika momwe anthu akugwirira ntchito ya khonsolo

2.1.5 Kulemba ndondomeko wa malonjezo a momwe khonsolo imagwilira ntchito zake

2.1.6 Kukhazikitsa ndi kuyendetsa thumba la ndalama lophunzitsira makhansala ntchito zosiyanasiyana

2.1.7 Kukhazikitsa ndondomeko yabwino yothandiza kuti azimayi nawo adzikhala pamaudindo akuluakulu.

## 2.2 Kupereka ntchito 38 zopindulira anthu amumzinda wa Lilongwe kudzera mu ndondomeko ya mgwirizano ndi makampani.

Khonsolo ikulephera kupereka ntchito zopindulira anthu mokwanira, motero kudzera mumgwirizano ndi makampani, ntchito zina zakhonsolo zidzigwiridwa ndi makampaniwo chifukwa ndi amene amakhala ndi ukadaulo wogwira ntchitozi. Khonsolo ikukhulupilira kuti ndondomeko imeneyi idzalimbikitsa mpikisano pakati pa makampani zomwe zidzapangitse kuti mitengo yogwilira ntchitoyi idzikhala yotsika. Chifukwa cha mavuto a zachuma komanso kulephera kutenga ngongole ku mabanki ndi mabungwe, Khonsolo yapanga chiganizo chopereka ntchito zake zina ku makampani ndi cholinga chakuti idzitha kulipira ndalama zochepa. Koma mgwirizano usanapangadwe, Khonsolo idzakhazikitsa ndondomeko zabwino ndi kuchita kauniuni kuti idziwe ngati kuli koyenera kutero, komanso idzaika ndondomeko zochitila kalondolondo wamomwe makampani akugwilira ntchito.

Magawo antchito okwana 38, ndiomwe adzaunikidwe ngati ndikoyenera kuwapereka ku makampani. Magawowa ndi awa;



Chipatala chaching'ono cha Chinsapo

### Kuyendetsa ntchito za pa ofesi

1. Kusamala malo ndi kukonza maluwa
2. Ntchito za alembi a pa ofesi
3. Kuyang'anira ntchito za magalimoto
4. Ntchito zotumikira pa ofesi
5. Kuinika ntchito zowona zamakopyuta komanso kusindikiza mapepala.
6. Ntchito zokonza magalimoto
7. Ntchito zokhudza zomangamanga
8. Ntchito zotolera ngongole
9. Ntchito zolandira maganizo a anthu komanso zothana ndi, katangale ndi ziphuphu.

### Ntchito zamalonda

10 Nyumba yogona alendo ya Lilongwe Guest House

11 Malo ochitira malonda a Wenela

12 Nyumba ya Chidzanja

13 Nyumba yochitira za nsangulutso (Lilongwe Town Hall) ndi ntchito zokongoletsa mitsinje (14) Malo ochitira masewera

15 Malo omwera mowa

16 Ntchito zodzala ndi kusamalira mitengo

### Za umoyo ndi misika

17 Kupereka ntchito zonse zoyendetsa ndi kusamalira zimbudzi zamadzi ku bungwe lowona za madzi la Lilongwe Water Board

18 Kuchotsa ndi kusamala zinyalala

19 Zimbudzi

20 Misika

21 Manda

22 Kusamala malo monga kutchetcha ndi kukonza mu ngalande

23 Ntchito yopima zinthu zosiyanasiyana

24 Malo osungira ziweto zomwe zalandidwa



Translated and designed by the Department of Information

## Ntchito za Mtengatenga

25 Malo oyimika magalimoto

26 Kukoka magalimoto omwe ayimitsidwa m'malo olakwika

27 Kusesa misewu pogwiritsa ntchito njira zamakono

28 Kukonza misewu

29 Kuperekera chakudya cha anthu ogwira ntchito yozimitsa moto

30 Kukonza malo oyimika magalimoto

31 Kusamalira malo ochezera

## Zomangamanga

32 Malo oyima mabasi

33 Msika wamakono

34 Zimbudzi zatsopano

35 Chitukuko chomanga nyumba

36 Kugwiritsa ntchito zinyalala popanga mphamvu yamagetsi

37 Manda atsopano

38 Malo amakono ophera ziweto

## Njira zokwaniritsira zimenzi

2.2.1 Kupereka ntchito zina kwa makampani

2.2.2 Kukhazikitsa ndi kuyendetsa ndondomeko yabwino yamomwe Khonsolo idzagwilire ntchito ndi makampani.

# 2.3 Kupeza ndalama zokwana K5 biliyoni kudzera mumgwirizano ndi mabungwe akunja komanso mabunwe omenyera ufulu wa anthu.

Ndi chachidziwikire kuti Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe siingakwanitse kuthetsa yokha mavuto omwe ikukumana nawo, motero ikuyenera kukhazikitsa ubale wabwino ndi boma, mabungwe ogwira ntchito zachitukuko ndi omeneya maufulu a anthu. Ubale umenewu udzathandiza kubweretsa pamodzi maganizo, luso komanso ndalama. Kuwonjezera pamanepa, ubale umenewu udzalimbikitsa ulamuliro wabwino zomwe zidzachititse kuti khonsolo idzipereka ntchito zapamwamba kwa anthu ake.

## Njira zokwaniritsira zimenezi

2.3.1 Kukhala ndi nthambi yomwe ntchito yake ndi kukhazikitsa ubale wabwino ndi okhudziwa.

2.3.2 Kulimbikitsa mgwirizano ndi Unduna wa Maboma Ang'ono komanso nthambi zina za boma ndi cholinga choonetsetsa kuti mfundo za boma zikutsatidwa

2.3.3 Kukhazikitsa ubale ndi mabungwe omenyera ufulu wachibadwidwe pofalitsa mauthenga okhudza zaumoyo, kulumikizana ndi anthu, kuteteza zachilengedwe, kupititsa patsogolo ntchito zamakampani ndi chisamaliro cha anthu.

2.3.4 Kupezera ndalama ndikugwira ntchito zachitukuko limodzi ndi mabungwe.



Galimoto yothandiza ngozi za moto



Translated and designed by the Department of Information

## 2.4 Kukonzanso ntchito za Khonsolo, kuthetsa mchitidwe wojomba pantchito komanso chinyengo pamalipiro

Kumayambiliro a chaka cha 2020, Khonsolo inalemba ntchito anthu okwana 1, 644 ndipo izi zinachitisa kuti ndalama zomwe zimagwiritsidwa ntchito zikwere ndi K43 pa K100 iliyonse ndipo ambiri mwa ogwira ntchitowa amenewa samagwiritsidwa ntchito bwino. Khonsolo ikuyenera kuchepetsa ndalama zomwe imalipira antchito ake kuti ithe kubweza ngongole komanso kumanga zinthu ndi kupereka ntchito zopindulira anthu. Ogwira ntchito akuyenera kukhala odalirika komanso adzigwira ntchito zomwe zili mmapulani a khonsolo. Vuto lomwe liripo ndi lakuti anthu ambiri ogwira ntchito amajomba mmene angafunire. Nthawi zina zimachitika kuti anthu 50 pa 100 ndiomwe amabwera ku ntchito zawo. Izi zili chomwechi chifukwa khonsolo ilibe kaundula odalirika wa anthu ake ogwira ntchito.

### Njira zothetsera mavuto amenewa ndi izi;

2.4.1 Kukonzanso kagwiridwe ka ntchito mogwilrizana ndi ntchito zomwe zilipo ndi kuonetsetsa kuti zikhale zopindulira anthu.

2.4.2 Kuchepetsa mchitidwe wojomba pantchito

2.4.3 Kukhala ndi kaundula odalirika wa anthu ogwira ntchito komanso kuti adzipuma dzaka zogwira ntchito zikakwana.

## 2.5 Kukhazikitsa njira younika mmene anthu akugwirira ntchito

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe ilibe ndondomeko zokhazikika zounikira momwe anthu akugwilira ntchito ndipo kufika pano, palibe ndondomeko yotsogolera kagwiridwe kantchito kogwirizana ndi dongosolo la zachuma. Kawirikawiri ndondomeko zakagwiridwe ka ntchito zimapangidwa popanda kutenga maganizo a anthu okhala mu mzindawu, komanso palibe mulingo woti tikwaniritse tikamagwira ntchito. Kuwonjezera pamenepa, palibenso ndondomeko zothandizira kupeza omwe akugwira ntchito bwino kuti apatsidwe mphoto.

### Njira zokwana zisanu zakhazikitsidwa kuti tithane ndi mavuto amenewa;

2.5.1 Kuonetsetsa kuti ndondomeko yakagwiridwe kantchito ikugwirizana bwino ndi ndondomeko yachitukuko komanso yachuma ya pachaka.

2.5.2 Kukhazikitsa gwirizano wakagwiridwe katchito ndi akuluakulu oyendetsa Khonsolo

2.5.3 Kukhazikitsa nthambi mu ofesi ya mkulu oyendetsa Khonsolo yomwe ntchito yake ndikuonetsetsa kuti mavuto akuthetsedwa, kauniuni ndi kalondolondo wa momwe ntchito ikugwiridwira akuchitika mosakondera ndipo ikuyenda bwino.

2.5.4 Kuonetsetsa kuti khonsolo ikupereka ntchito kwa anthu okhala mu mzindawu mu nthawi yoikika mogwirizana ndi lonjezo la kagwiridwe kantchito.

2.5.5 Kupereka mphoto kwa anthu amene akugwira ntchito bwino mu njira yoyeserera.



Translated and designed by the Department of Information

# GAWO LACHITATU:
# **KUPEREKA NTCHITO KWA ANTHU**

Mavuto azachuma omwe khonsolo ikukumana nawo asokoneza kwambiri kagwiridwe kantchito. Mwachitsanzo, pakadali pano khonsolo ikungokwanitsa kuchotsa zinyalala mwa zinyalala zambiri zomwe zimatayidwa mu malo osiyanasiyana. Kuonjeza pamenepa, zipatala za khonsoloyi zimalandira ndalama zochepa zogwirira ntchito. Misewu ya mu mzindawu nayo ilibe magetsi okwanira ndipo pamapita nthawi yaitali kuti misewu yomwe yaowongeka ikonzedwe. Khonsoloyi ikulepheranso kuthandiza mokwanira makampani omwe ndi nsanamila yothandiza kukweza chitukuko cha mu mzindawu. Mzindawu ulibenso malo okwanira ochezera ndipo mitsinje ndi malo ena anthu akulowerera. Sukulu za pulaimale zili ndi ana ophunzira ochuluka kwambiri, zimene zimachititsa kuti ana ambiri adzibwereza kalasi komanso kusiyila sukulu panjira.

Ndondomeko imeneyi ikupereka chitsogozo cha momwe Khonsolo isintire zinthu zake. Mwachitsanzo ndalama ndi zipangizo ziyenera zizipita ndi kugwritsidwa ntchito ku magawo ofunikira kwambiri. Kuti zonsenzi zitheke pakufunika kudzipereka ndi kulimba mtima pakati pa anthu ogwira ntchito.

## Cholinga chachikulu cha gawo limeneli

Kugwira ntchito mwaukadaulo pogwiritsa ntchito zipangizo (ndalama) mosamala pofuna kupititsa patsogolo nchito zamakampani, kuteteza chilengedwe, kusamala zinyalala, kukhala ndi mayendedwe abwino, kukonza dongosolo la zaumoyo komanso maphunziro.

## Zolinga zazing’ono

1. Kupititsa patsogolo ntchito zamakampani
2. Malo ochezera ndi chilengedwe
3. Kusamala zinyalala
4. Ntchito za mayendedwe
5. Za umoyo
6. Ndondomeko yachitukuko cha mumzinda
7. Ndondomeko yokhazikitsa ntchito zamalonda
8. Maphunziro



Malo ochezera



Ntchito yoyika magetsi a mumsewu

## 3.1 Kukweza chuma ndi kuthandiza magulu azamalonda omwe sali mkaundula waboma okwana 1, 600



Translated and designed by the Department of Information

Pofuna kukweza chuma cha mu mzindawu, Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe yayika chidwi chake pa ntchito zoyendetsa misika komanso kupereka ziphaso zabizinesi. Izi ndi zosakwanira pantchito yofuna kukweza chuma cha Mzinda wa Lilongwe. Tsopano ndi nthawi yakuti khonsoyi ithandize makampani kuthetsa limodzi mavuto, kupeza limodzi ndalama, kupititsa patsogolo ntchito zomangamanga, kutukulu luso la bizinesi ndi kulimbikitsa mpikisano pakati pa makampani.

Ndondomeko iyi ikuimira mfundo za khonsolo zofuna kupititsa patsogolo ntchito za makampani.

### Mfundozi zomwe ndi zisanu zili motere;

3.1.1 Kukhala ndi misonkhano 6 pa chaka ndi ochita ntchito zamalondo ndicholinga chofuna kupeza mwayi wa mabizinesi komanso kuthetsa zotsamwitsa zomwe makampani amakumana nawo.

3.1.2 Kupititsa patsogolo ntchito zoyendera madera a mzinda

3.1.3 Kuthandiza mavenda okwana 1,000 ndi anthu otola zinthu zotayidwa

3.1.4 Kulimbikitsa a mabizinesi okwana 300.

3.1.5 Kupereka thandizo la ndalama kwa a malonda 400 omwe sali mkaundula waboma kudzera mundondomeko yangongole yomwe ikuyendetsedwa ndi mabungwe omwe siaboma kapena obwereketsa ndalama.

## 3.2 Kukulitsa malo ndi ndikuteteza zachilengedwe

Zachilengedwe mumzinda wa Lilongwe ziri pachipsezo chachikulu. Pafupifupi mitsinje yonse ya mu mzindawu anthu analoweleramo ndi kudula mitengo. Mitsinjeyi siyotetezeka ndipo anthu akulimamo. Ena amatailako zinyasi pamene ena amafukulako mchenga. Ngakhale Lilongwe uli Mzinda wokongola, uli ndi malo ochepa osamalira zachilengedwendi komanso kochezerako. Malo ocherzera omwe alipo ndi osakonzedwa ngakhale panali dongosolo lofuna kutero mmadera a Area 18, Area 49 ndi Eden ku Area 13.

### Pofuna kuteteza ndi kusamala zachilengedwe khonsolo yakhazikitsa njira izi:

Njira zomwe takonza ndizofuna kuteteza mitsinje, chilengedwe, kudzala mitengo mbali mwamitsinje, komanso kulimbikitsa kubyala mitengo mmalo a anthu.

3.2.1 Kupereka zipangizo zogwilira ntchito ku ofesi yoyendetsa ntchito zachilengedwe kudzera mmapolojekiti kumanso mgwirizano ndi mabungwe osiyanasiyana.

3.2.2 Kukhazikitsa malo atsopano ochezera okwana 100 hekitala .

3.2.3 Kuteteza madambo ndi malo a mmbali mwa mitsinje okwana 200 hekitala

3.2.4 Kubwezeretsa nkhalango ndi mitengo yobwezeretsa chonde munthaka okwana 500 hekitala

## 3.3 Kuchotsa ndi kutaya zinyala ku malo oyenera

Anthu ambiri amataya zinyala mmalo osayenera, mbali mwamitsinje ndi mmbali mwa misewu. Zinyala zambiri zimaotchedwa kapena kutayidwa mudzala, zimene zimabweretsa mpweya oyipa. Kafukufuku yemwe Khonsoloyi inachita mchaka cha 2017 anaonetsa kuti zinyala zochepa zokha ndi zimene zimachotsedwa mu malo osiyanasiyana. Zimenezi ndi zosiyana kwambiri poyerekeza ndi mizinda ina ikuluikulu ya muno mu Afilika.



A Kaduya kutsogolera ntchito yosesa mumzinda wa Lilongwe



Translated and designed by the Department of Information

### Njira zothetsera mavuto amenewa

3.3.1 Kukonza dongosolo labwino la ntchito zachitukuko ndi kukhazikitsa malamulo othandiza kubweretsa ukhondo mu mzindawu

3.3.2 Kulongosola momveka bwino ndondomeko yapezera ndalama zogwilira ntchito yosamala zinyalala komanso kukhala ndi chithunzithunzi cha ndalama zimene zingafunike pogwira ntchito imeneyi

3.3.3 Kupeleka theka la ntchito yochotsa zinyalala mmakomo kwa anthu a mabizinezi

3.3.4 Kusankha zinyalala ndi kuzikonzanso ndicholinga chofuna kuzigwiritsa ncthito ngati mphamvu ya magetsi Makala komanso mapepala

3.3.5 Kuyendetsa ntchito za malo otayira zinyalala mwaukadaulo mogwirizana ndi makampani

## 3.4 Kukhala ndi misewu yabwino ndi yamakono

Kuchuluka kwa magalimoto poyelekeza ndi misewu zakhudza kwambiro ntchito za mtengatenga. Ngalande nazo ndizosalongosoka ndipo izi zapangitsa kuti misewu yambiri ikhale yoonongeka. Misewu yambiri ndi yokumbika zomwe zikuchulukitsa chiwerengero changozi zapamsewu. Ma basi ang'onoang'ono (mini-buses) amayenda mosatsata malamulo a pamsewu. Kuwonjezera pamenepa magetsi a mmisewu ya mumzindawu ndiochepa komanso amawonongedwa ndi anthu.

Ngakhale zinthu zili chomwechi, khonsolo iyesetsa kugwiritsa ntchito ndalama zomwe imapeza pobwezeretsa magetsi mmisewu, kupitsa patsogolo ntchito zamtengatenga, powonetsetsa kuti malamulo a pamsewu akutsatidwa, kuchepetsa ndalama zogwirira ntchito posesa misewu komanso kukonza misewuyi.

### Njira zothetsera mavuta amenewa

3.4.1 Kulimbikitsa upangiri wa khonsolo ndi kayendetsedwe ka ntchito za mtengatenga

3.4.2 Kukonzanso magetsi ammisewu komanso kuika magetsi oyendera mphamvu yadzuwa pa mtunda wokwana makilomita 40, komanso kuonetsetsa kuti magetsi akuyaka pa mtunda wokwana makilomita 75

3.4.3 Kuchepetsa vuto lakuchuluka kwa magalimoto ndi kuonetsetsa kuti pali dongosolo labwino lakayendedwe kabwino ka pamsewu

3.4.4 Kusesa theka la misewu ya mu mzindawu pogwiritsa ntchito galimoto zamakono zokhala ndi makina osesera

3.4.5 Kukhazikitsa nthambi yomwe idzikonza ndikukwilira mayenje mmisewu yonse pafupifupi kamodzi pachaka

3.5 Kuchepetsa mlili wa COVID 19, kulimbikitsa ntchito za umoyo, chisanmaliro cha ana ndi uchembere wabwino

## 3.5 Kuchepetsa mlili wa Covid-19, kulimbikitsa ntchito za umoyo, chisamaliro cha ana ndi uchembere wabwino

Khonsola ya Mzinda wa Lilongwe ili ndi udindo wopereka ndondomeko zopewera matenda osiyanasiyana. Pachifukwa chimenechi, ndondomeko iyi ilunjika pa mfundo izi; kulimbana ndi mlili wa Covid-19, ukhondo wa madzi ndi chakudya, uchembere wabwino ndi umowo wa ana. Khonsolo ikuyenera kutenga mbali yaikulu polimbana ndi mlili wa Covid-19 powonetsetsa kuti anthu akutsatira njira zopewera matendawa.

Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe ili ndi zipatala zing'onozing'ono khumi zomwe sonse pamodzi zinathandiza anthu okwana 16,302 pakati pa chaka cha 2019 ndi 2020. Ngakhale ana okwana 48,000 amabadwa pa chaka mu mzindawu, ndizokhumudwitsa kuti anthu ochepa okha ndiomwe akugwiritsa ntchito zipatala khumi zimenezi. Kuwonjezera pamenepa, ntchito yoyendera anthu amene amapanga bisinesi yophika zakudya komanso makampani omwe amatayira zinyansi ndi yochepa kwambiri.

### Njira zothetsera mavutowa

3.5.1 Kulimbikitsa anthu kukhala motalikana komanso kufalitsa mauthenga opewera matenda a Covid-19.

3.5.2 Kulimbikitsa ntchito zaumoyo ndi ntchito zoyeza madzi, chakudya ndi zinyasi za mmafakitale.

3.5.3 Kupereka ntchito zokwanira za uchembere


Translated and designed by the Department of Information

wabwino ku zipatala zathu zokwana 8 komanso kuonetsetsa kuti anthu ambiri akupeza chithandizo cha zaumoyo pofika mchaka cha 2024/2025.

## 3.6 Kuthandiza mabanja okwana 25,000 kukhala ndi nyumba, malo ovomerezeka ndi kutsilizitsa ndondomeko zinayi za chitukuko

Kuchuluka kwa anthu okhala mu mzindawu kwachititsa kuti nyumba zikhale zoperewera komanso anthu ena adzikhala mmalo osayenera. Ndipo anthu ambiri okhala mmadera a mu mzindawu akusoweka ukhondo ndi, madzi abwino komanso.. Podziwa kuti ntchito za malo zimayendetsedwa ndi boma, khonsolo ya mzindawu ilunjika panchito yomanga nyumba zambiri, kuika mchimake umwini wamalo, komanso kukhazikitsa ndondomeko zapamwamba zachitukuko.

### Njira zomwe Khonsolo itsatire ndi izi;

3.6.1 Mothandizana ndi makampani, kukhazikitsa ntchito zomanga nyumba zokwana 15,0000 kuti zipindulire mabanja osauka

3.6.2 Kuthandiza mabanja 10,000 kukhala mmalo ovomerezeka

3.6.3 Kuonetsetsa kuti malo a Area 59 ndi Area 62 akhala mbali imodzi ya Mzinda wa Lilongwe.

3.6.4 Kukhazikitsa ntchito imodzi yachitukuko pa chaka yobweretsa kusintha kwakukulu mu mzindawu

## 3.7 Kupeza ndalama ndi kukhazikitsa ntchito ya chitukuko yokwana $20 million

Ngakhale Khonsolo ya Mzinda wa Lilongwe ili ndi zitukuko zomangamanga zambiri, zitukukozi ndi zosakwanira. Khonsoloyi ilibe ndondomeko yokhazikitsira ntchito zikuluzikulu za chitukuko. Zitukuko zimenezi ndizofuna thandizo la ndalama zochuluka kuchokera ku mabungwe akunja komanso kudzera mumgwirizano wa boma ndi mabungwe obwereketsa ndalama. Koma ndalamazi zikhoza kupezeka ngati khonsoliyi ingasinthe kagwiridwe ka ntchito zake komanso kukhala ndi mbiri yabwino.

### Ndondomeko zokwaniritsa zimenezi ndi izi;

3.7.1 Kukhala ndi kaundula wa zitukuko zomangamanga zomwe zilipo

3.7.2 Kulemba ndikuika mukaundula zitukuko zomangamanga zomwe tingamange moyambilira, kudzera mukukambirana ndi okhudzidwa.

3.7.3 Kukhala ndi kaundula wa zitukuko

3.7.4 Kupeza ndalama zokhazikitsira ntchito zachitukuko mogwirizana ndi mabungwe ogwira nawo ntchito.

## 3.8 Kukweza ntchito zamaphunziro popeleka thandizo la ndalama kuchekera kuthumba la Khonsolo zokwana K400 million

Sukulu za mumzinda wa Lilongwe zikukumana ndi mavuto ambiri. Kusiyana pakaperekedwe kazipangizo ku sukulu lakhala bvuto lalikulu. Mwachitsanzo, Ana ophunzira alipo ambiri poyerekeza ndi aphunzitsi. Kuwonjezera pamenepa, adindo amayendera sululuzi mwapatalipatali. Mchaka cha 2020, sukulu 36 pa 100 zaboma ndizomwe zinayenderedwa ndipo kuyendera kumeneku kunapeza kuti sukulu 8 mwa 100 ndizomwe zimapereka maphunziro bwino.

Chifukwa china ndi kuchepa kwa zipangizo monga makalasi komwe kwachititsa kuti kalasi imodzi idzikhala ndi ophunzira ochuluka kuposa muyeso wake. Vuto lina ndikuchepa kwa aphunzitsi ophunzitsidwa bwino komanso zipangizo zophunzilira komanso kuchepa kwa nambala ya ana omwe amalembetsa kuti ayambe sukulu. Kafukufuku wawonetsa kuti ana ambiri amabwereza kalasi chifukwa okhoza kupita kalasi ina amakhala ochepa.

### Pofuna kuthana ndi mavuto amenewa, Khonsolo yaika njira izi;

3.8.1 Kukhazikitsa ndi kuyendetsa thumba la ndalama la zamaphunziro

3.8.2 Kumanga makalasi okwana 30 ndi zimbudzi



Translated and designed by the Department of Information

zokwana 100 mogwirizana ndi anthu akudera.

3.8.3 Kupereka mabuku ophunzitsira okwana 10, 000 komanso ma mipando yokwana 1,500.

3.8.4 Kuonetsetsa kuti aphunzitsi okwana 200 aowonjezera maphunziro awo

3.8.5 Kupereka upangiri kumakomiti 20 oyendetsa ndi kuyang'anira sukulu

3.8.6 Kuonetseta kuti sukulu zikuyenderedwa kamodzi pachaka



Mkumano wa khonsolo ya mzinda wa Lilongwe

## 3.9 Kupezera ntchito achinyamata okwana 10,000 ndikubweretsa mipikisano yosiyanasiyana kwa anthu okwana 50,000

Anthu ambiri okhala mu mzinda wa Lilongwe ndi achinyamata.

Chiwerengero cha anthu chimene chinachitika mchaka cha 2018 chinawonetsa kuti athu opitilira theka ndi azaka zoyambira 10 kufika 35. Ngakhale kuti chiwerengero cha athu ambiri ndi cha achinyamata, achinyamatawa amasowa zinthu zambiri zimene zingathandize kupititsa patsogolo miyiyo yawo. Kuphatikiza kusowa kwa ndondomeko zachitukuko za achinyamata, palibe malo okwanira ochitira masewero ndipo mipikisano ndiyochepa. Achinyamata amakumana ndi mavuto osiyanasiyana kuphatikizapo kukwera kwa chiwerengero cha amene amasiyira sukulu panjira, kusowa kwa luso ndi mwayi wantchito komanso amakumana ndi nkhanza zosiyanasiyana.

### Njira zothetsera mavuto amenewa ndi izi;

3.9.1 Kupeza chuma chochuluka ndi upangiri othandiza kukweza ntchito za achinyamata ndi masewero

3.9.2 Kukhazikitsa ntchito zimene zingapindulire achinyamata okwana 10,000 pofika cha 2025

3.9.3 Kumanga malo atsopano a achinyamata ochitira masewero osiyanasiyana

3.9.4 Kukhazikitsa malo azamasewero osiyanasiyana pafupifupi mmasukulu onse a pulayimale

3.9.5 Kuyendetsa mipikisano ya masewero osiyanasiyana okwana 10,000 pofika mchaka cha 2025

3.9.6 Kukhazikitsa malo amodzi azamasewero amumzindawu



Translated and designed by the Department of Information